

MWAZI

*"Pakuti moyo wa
nyama ukhala
m'mwazi; ndipo
ndakupatsani uwu pa
guwa la nsembe, ucite
cotetezera moyo wanu;
pakuti wocita cotetezera
ndiwo mwazi, cifukwa
ca moyo wace."*

(Levitiko 17:11)

Cosowa cacikulu ca munthu.

Tcimo lalekanitsa munthu ndi Mulungu kukhala wolekana ndi Mulungu kutanthauza kukakhala mugehena nthawi zosatha, cifukwa Mulungu sadzalekerera tcimo, ndipo tcimo liyenera kulangidwa. Munthu ndi wocimwa koma Mulungu ndi woyera. Mwazi wa Yesu Kristu ndiyo njira ya Mulungu yokwaniritsa cosowa cacikulu ca munthu.

Nsembe yaikulu ya Mulungu.

Mulungu adatuma mwana wake, Ambuye Yesu Kristu, kudzafa pa mtanda kukhala dipo la macimo anu. *“amene Mulungu anamuika poyera akhale cotetezera mwa cikhulupiriro ca m’mwazi wace...”* (Aroma 3:25) Zindikirani kuti cidali cikonzero ca Mulungu osati ca munthu: *“amene Mulungu anamuika...”* Kaciwiri, zindikirani kuti Kristu adafa kuti alipire macimo athu. *“akhale cotetezera...”* potsirizira ndimeyi ikunena kuti cikhululukiro cimalandilidwa pakungokhulupilira zimene Yesu adazicita. *“mwa cikhulupiriro ca m’mwazi wace...”* Cifukwa ca mwazi, Mulungu angathe kuonetsa cifundo kwa ocimwa, pokhalabe oyera ndi olungama. *“...kuti lye akhale wolungama, ndi wakumuyesa wolungama iye amene akhulupirira Yesu.”* (Aroma 3:26)

Kodi mwazi wa Yesu udzacita ciyani?

1) Mwazi umatsuka kuyeretsa inu ku macimo. *“...Kwa lye amene atikonda ife, natimasula ku macimo athu ndi mwazi wace.”* (Cibvumbulutso 1:5) *“ndipo mwazi wa Yesu Mwana wace utisambitsa kucitotsera ucimo wonse.”* (1 Yohane 1:7)

2) Mwazi umalipira za cikhululukiro canu. *“Tiri ndi maomboledwe mwa mwazi wace, cikhululukiro ca zocimwa,”* (Aefeso 1:7)

3) Mwazi umabweretsa mtendere ndi Mulungu. *“mwa lyenso kuyanjanitsa zinthu zonse kwa lye mwini, atacita mtendere mwa mwazi wa mtanda wace...”* (Akolose 1:20)

4) Mwazi umakupulumutsani inu ku mkwiyo wa Mulungu. *“Ndipo tsono popeza inayesedwa olungama ndi mwazi wace, makamaka ndithu tidzapulumuka mkwiyo wa Mulungu mwa lyeyo.”* (Aroma 5:9)

5) Mwazi umatsegula njira ya kumwamba. *“Ndipo pokhala naco, abale, cilimbikitso cakulowa m'malo opatulika, ndi mwazi wa Yesu,”* (Ahebri 10:19)

Muyenera kucita ciyani?

1) Bvomezani cosowa canu. *“pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu;”* (Aroma 3:23) *“Cifukwa ndazindikira macimo anga...”* (Masalmo 51:3) *“Nditenga nkhawa cifukwa ca cimo langa.”* (Masalmo 38:18)

2) Khulupilirani mwatunthu malonjezano a Mulungu. *“Ukhulupilire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka...”* (Macitidwe 16:31) *“Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu; cosacokera kuntchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense.”* (Aefeso 2:8,9) *“podziwa kuti simunaomboledwa ndi zobvunda, golidi ndi siliva, kusiyana nao makhalidwe anu acabe ocokera kwa makolo anu: koma ndi mwazi wa mtengo wace wapatali monga wa mwana wa nkhusa wopanda cirema, ndi wopanda banga, ndiwo mwazi wa Kristu.”* (1 Petro 1:18, 19)

3) Lirani kwa Mulungu mupemphero. *“...Mulungu, mindicitire cifundo, ine wocimwa.”* (Luka 18:13) *“pakuti, amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka.”* (Aroma 10:13)

Kusankha kwanu kwakukuru.

Yesu adakhetsa mwazi wake, adaikidwa m'manda, ndipo adaukansa pa tsiku la citatu. Pakadali pano ali okonzeka kuti akupulumutseni inu. Kusankha kuli kwa inu. Nyimbo imati, "Ngati mwazi, wa Kristu uli wokwanira kwa Mulungu, zoonadi ndithu, uli wokwaniranso kwa ine." Ndi mwazi umene umakwaniritsa Mulungu. Cifukwa ciyani osaika cikhulupiro canu muntchito imene adaitsiriza Kristu ndi kumuitana lye kuti akupulumutseni? *"kucokera komweko akhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa lye, popeza ali nao moyo wace cikhaliire wa kuwapembedzera iwo."* (Ahebri 7:25) *"...Yesu Kristu...atikonda ife, natimasula ku macimo athu ndi mwazi wace."* (Cibvumbulutso 1:5)

Conde tuma traki lino kwa ife kuti tidziwe ngati wasankha kukhulupirira Yesu Kristu kukhala Mpulumutsi wako utawerenga trakili.

Dzina _____

Keyala _____

Zaka _____

Foni _____



FELLOWSHIP TRACT LEAGUE

P.O. BOX 164 • LEBANON, OH 45036

www.fellowshiptractleague.org © Tract 8076 (Chichewa)

All tracts free as the Lord provides. Not to be sold.